BWERANI AZIMAI

Bwerani Azimai
Konse lalikani
Muyimbeni
Kristu ndiye M'lungu
Kristu anauka
Kristu ndiyè nyali
Tamandani

Bwerani ana onse
Ndi alongo onse
Phunzitsani
Kuli wodwala
Akufokafoka
Akukhala mdima
Pempherani.

Gwirani nchito zanu
Limbikani ndi mphamvu
Mupatseni
Cikondano canu
M'tima idzakondwa
Ndi cikondi cace
Tiyembekeze.

Ngati tidzazituta
Mulungu atipatsa
Muzambiri
Kristu wofatsa
Onse adzamfuna
Alimphoto yathu
Ndi cotsata.

BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P. O. BOX 1995
LUSAKA, ZAMBIA

7100

# ZIPHUNZITSO ZA YESU



W 143
NYA

TEACHINGS OF JESUS
BAPTIST WOMEN OF ZAMBIA
(CHINYANJA)

Published by
The Baptist Publishing House
P. O. Box 1995
Lusaka, Zambia

1 October 1977

Printed by
Baptist Printing Ministry
P. O. Box 1995
Lusaka, Zambia

tiyenera kucita, ndipo ngati tilephera ndiye kuti timacimwila Mulungu. (Werengani Yakobo 4.17).

Timabela Mulungu ngati sitipereka cacikhumi kwa iye. (Werengani Malichi 3.8-9). Kodi mukhulupilira kuti kubela munthu wina ndi mlandu waukuru? Umakhala mlandu waukuru pamene tibela Mulungu.

Mwina muli kulankhula kuti, "Mulungu adziwa kuti ndifuna kupereka cacikhumi ndipo tsiku lina ndi zatero." Iai, Mulungu safuna akuti "Ndakupatsani zinthu zambiri. Ndifunsa cabe kuti mukhale okhulupirika ndi kundipatsanso kwa ine."

Anthu ena amapatsa kupitilila limodzi la magawo khumi kamba ka cikondi, cimene cimaonetsedwa kulingana ndi mmene tipatsira. Tiyeneranso kuzipereka ife eni. Ngati tizipereka ife eni, ndiye kuti nthawi ndi nthawi tidzazindikila kuti zonse zomwe tiri nazo zicokera kwa Yesu Kristu.

MTSOGOLERI:

Mau awa atiuza zinthu zoyenera lero. Mwina ena aife sitinamve mau awa kale. Koma tsopano tidziwa.

Kodi tsopano simungapange pangano ndi Mulungu kuuza iye kuti kucokera tsopano ndizakhala ndili kupereka cacikhumi? Pempherani kuti Mulungu akukhululukileni kamba kakuti munalephera kale kupereka cacikhumi.

Tikhoza kuyamba kucita zinthu zimene Mulungu afuna ife kuti ticite.

PEMPHERO:

(1 Akorinto 9.13-14).

Nchito ina ya ndalamazo zomwe zipereke-dwa ku mpingo ndikugula mabuku akuphunzitsamo anthu ndi kusunga nyumba yopempherer amo bwino.

GAWO IV:

Anthu amene anakhala mnthawi ya Mcipangano Cakale anatsatira mau awa monga lamulo. Anabvomekeza za lamulo kamba kakuopa Mulungu ndi cilango cace. Tawerenga mau akuti linali lamulo la Mulungu kuti anthu apereke cacikhumi. Conco anthu a Mulungu anatsatira lamulo limenelo ndipo anali okhulupirika kupereka cacikhumi.

Mcipangano Catsopano Yesu akuti, "Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula cilamulo kapena aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa." (Mateyu 5.17). Ziphunzitso za Yesu zinapitilira pa lamulo.

Mkristu sayenera cabe kucita zomwe lamulo linena motero kuti asalangidwe. Koma kuti akhale mu mzimu wa lamulo kamba ka cikondi cace kwa Yesu Kristu. Kupatsa kwathu kwa cacikhumi kuyenera kuti kukhale tero kamba ka cikondi cathu kwa Yesu Kristu. Anacicitira zambiri. Ndipo ife timacitira zing'ono (Werengani 2 Akorinto 9.6-8).

GAWO V:

Kodi ndi ucimo ngati sitipereka cacikhumi kwa Mulungu? Inde. Buku Lopatulika litiuza kuti ngati tidziwa cabwino cimene



ZIPHUNZITSO ZA YESU


| MUTU | | TSAMBA |
|---|---|---|
| 1. | KUDZIWA MULUNGU | 1 |
| 2. | PEMPHERO | 7 |
| 3. | KUPEMPHELERA PAMODZI | 12 |
| 4. | UFUMU WA MULUNGU | 17 |
| 5. | KUUNIKA | 22 |
| 6. | NGOZI MMOYO WOPANDA MZIMU | 28 |
| 7. | CIKONDWELERO | 33 |
| 8. | KUDZICEPETSA | 39 |
| 9. | CHUMA | 45 |
| 10. | UDINDO WA MKRISTU MMOYO | 51 |
| 11. | UDINDO WAKUPATSA | 56 |

MUTU 1

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: KUDZIWA MULUNGU

MAU APAMTIMA: *"Koma moyo wosatha ndi uwu, kuti akadziwe Inu Mulungu woona yekha, ndi Yesu Kristu amene munamtuma."*
*Yohane 17.3*

MTSOGOLERI:

Kodi munazifunsapo kale nokha, "Kodi ndine yani? Ndi cifukwa ninji ndiri padziko lino?" Anthu kwa nthawi yaitali akhala ali kufunsa mafunsowa. Mlembi wa Masalmo anafunsa mu Masalmo 8.4, "Munthu ndani kuti mumkumbukila? Ndi mwana wa munthu kuti muceza naye?"

Mu Genesis 1.26a tiwerenga kuti: "Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'cifanizo cathu, monga mwa cikhalidwe cathu....." Kodi ici citanthauza ciani kulengedwa mcifaniziro ca Mulungu? Pali zinthu zitatu zimene zitipanga ife kukhala ngati Mulungu. Anatipatsa nzeru, kumvera ndi cifunilo. Kupyolera mzinthuzi tikhoza kuganizira ndi kuona zinthu ndi kusankha.

Pamene Mulungu anapatsa munthu zinthu izi, anali kupanga munthu amene iye akanakonda. Anafuna wina wakuti amkonde. Ndipo anafunanso wina kuti akonde iye Mulungu. Sicikanakhala cikondi coona ngati tinapangidwa monga makina (machine). Tiyenera kuyankha Mulungu ndi nzeru zathu zonse moyenera.



mu mau athu apamtima.

"Mai Mariya anali Mkristu amene anagwilira nchito mzungu kuti apeze ndalama, koma anapeza lingo mmene iye akanapezera ndalama zopereka kwa Mulungu. Mai Mariya anapeza ganizo lakugulitsa ndiwo, kufesa zipatso ndi madzila kucokera ku nkhuku.

Mmenemo ndimo mmene mai Mariya anapezera ndalama zopereka kwa Mulungu, mkugulitsa matomato, madzila ndi ndiwo zocokera mdimba. Izi ndi ndalama ziri kugwiritsidwa nchito mu mpingo."

GAWO III:

Kodi cacikhumi ciyenera kugwiritsidwa nchito mchalichi mnjira yotani? Cacikhumi ciyenera kugwiritsidwa nchito mnjira ya kupereka nchito ya Mulungu patsogolo. Mpingo uli ndi nchito zambiri zocita. Conco cacikhumi ciyenera kugwiritsidwa nchito mzinchito zoyenera.

Mbusa ayenera kulipiridwa ndalama zocokera ku cacikhumi. Ici cinali coona ngakhale mcipangano cakale. (Werengani Numeri 18.24, dziwani kuti alevi anali ansembe).

Tiphunzilanso zolipira mbusa Mcipangano Catsopano. "Kodi simudziwa iwo akutumikira za kacisi amadya za m'Kacisi, ndi iwo akuimirira guwa la nsembe, agawana nalo guwa la nsembe? Comweconso Ambuye analamulira kuti iwo amene alalikira Uthenga Wabwino akhale ndi moyo ndi Uthenga Wabwino.

khumi pa zomwe tilandila. Izi ndalama zomwe tilandila, cakudya ndi zina zace. Tikhoza kulandila izi pakugwira nchito. Tikhoza kukhala ndi izi pa kukhala ndi malonda athu eni. Zonsezi ziri madalitso ocokera kwa Mulungu. Ayembekezera kuti tionetse cikondi ndi kuyamika iye Mulungu pakupereka cacikhumi kwa iye.

Cacikhumi ciri mnjira ya Mulungu yakugwiriramo nchito mchalichi pano pa dziko lapansi. Munthu wina anali ndi cacikhumi ndi njira ya Mulungu ya kuphunzitsilamo ana ace kumvera zomwe iwo ayenera kucita.

Ndalama ya cakhumi idzakhala yosiyana kamba kakuti sitilandila cimodzi modzi. Koma pa zonse cizakhala ciri kuperekedwa mnjira imodzi ya limodzi la magawo khumi. Ngati mulandila K10.00, muyenera kupereka K1.00 kwa Mulungu.

GAWO II:

Kodi ndani amene ayenera kupereka cacikhumi? Kodi ndi iwo okha amene ali wokonzeka kapena amene ali okhulupirika? Kodi wina anganene kuti "Ndili wosauka conco Mulungu sayembekezera cacikhumi kwa ine?

Mafunso awa ali kufunsidwa nthawi zambiri. Kodi ndani angayankhe izi? Buku Lopatulika ndi mau a Mulungu amene alankhula kwa ife. Buku Lopatulika likuti onse anthu ali kulamulilidwa kupereka cacikhumi. Timalandila kucokera kwa Mulungu. Conco tiyenera kuperekanso zomwe Mulungu atipatsa, Yesu akuti sitiyenera kukana kupereka cacikhumi



GAWO I

Tidziwa kuti mwamuna woyamba ndi mkazi onsewa anatembenukila kwa Satana kucokera kwa Mulungu. Iwo sanamvere ai. Anasankha kuti asatsatire Mulungu. Mulungu sanawakakamize kuti amkonde. Ndipo Mulungu satikakamiza ife kuti timkonde.

Koma mtima wa Mulungu uyenera kuti unali wacisoni. Anafuna mwamuna ndi mkazi kuti akonde Mulungu. Popeza munthu anasankha njira ya iye mwini, mzimu wa Mulungu sunkakhala mwa munthu uja ndi kukhala mciyanjano ndi Mulungu. Mzimu wa Mulungu unacoka mu mtima wa munthu. Tsono munthu anafa mwa uzimu, monga Mulungu anakambila kuti cidzacitika ngati munthu sankamvelera iye Mulungu. (Werengani Aefeso 2.1).

Kodi Mulungu adzacita ciani tsopano? Anali ndi njira yabwino. Ankatumiza mwana wace amene akanalipila mtengo wa macimo a munthu. Tsono iye amene asankha kulandila mphatso ya Mulungu, iye amasankha cikondi ca Mulungu. Macimo ace ankakhululukiiidwa. Akanakhala woyera.

Mzimu wa Mulungu tsono ukanabwela kukhala mwa iye mumtima, Iye akhoza tsono kukhala wamoyo mu mzimu. Iye akhoza tsono kukhala ndi moyo womwe sunkanatha.

GAWO II:

Cifukwa Mulungu analenga munthu kuti amkonde ndikutinso akonde Mulungu, munthu adziwa kuti ali opambana mwa thupi lokha.

Adziwa kuti aliko amene apambana munthu. Iye ali naco cifuno cakufuna kuona kuti kodi ndani. (Werengani Afilipi 3.10).

Anthu ambiri sadziwa kuti cifuno ici mmitima yawo ciri cotani. Adziwa cabe kuti sangathe kupeza mtendere. Amayesa njira zambiri komabe sapeza mtendere. Akhoza kuyesa kupeza mtendere pakumwa mowa, njuga, ndi kucita zinthu zina.

Kodi tingadziwe bwanji Mulungu? Tawerenga kale za njira ya Mulungu ya kubweretsa munthu kucokera ku cimo ndi kupita kwa iye. Tikhoza kumvelera Mzimu wa Mulungu uli kulankhula mmitima yathu. Umatiuza za mlandu wathu kamba ka macimo. Umatiuza kuti, cifukwa Mulungu atikonda, atipezera njira kuti tithawe kucokera ku imfa ya macimo athu.

Pamene tilandila Yesu Kristu monga Mpulumutsi wathu, timabvomekeza cikondi ca Mulungu cacikuru. Pamene tilandila cikhululukilo ca macimo athu, Mzimu wace ukhoza kukhala mwa ife. Pamene ici cicitika, timakhala ndi moyo wosatha. Kodi moyo wosatha ndi uti? Mau athu apamtima anena kuti ndi kudziwa Mulungu ndi mwana wace Yesu Kristu.

GAWO III:

Kodi tingamdziwe bwanji Mulungu? "Pakuti popeza m'nzeru ya Mulungu dziko lapansi, mwa nzeru yace, silinadziwa Mulungu, cidamkonda Mulungu kupulumutsa okhulupirawo mwa copusa ca kulalikira." (1 Akorinto 1.21) Paulo ali kulankhula kuti sitingadziwe Mulungu kupyolera mnzeru zathu eni. Colinga cace ndi kupulumu-



MUTU 11

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: UDINDO WAKUPATSA

MAU APAMTIMA: *"Tsoka inu, alembi ndi Afarisi, onyenga! cifukwa mupereka limodzi la magawo khumi la timbeu tonunkhira, ndi katsabola, ndi la citowe, nimusiya zolemera za cilamulo, ndizo kuweruza kolungama, ndi kucitira cifundo, ndi cikhulupiriro; koma zijazo munayenera kuzicita, osasiya izi zomwe."*

*Mateyu 23.23*

MTSOGOLERI:

Phunziro lathu lalero liri loyenera kwambiri, udindo wakupatsa. Timalandila madalitso a Mulungu ambiri kweni kweni, Tsono nanga ife kupatsa Mulungu? Kodi mumaona kuti coyenera? Kodi Mulungu ayembekezera ciani kucokera ku ana ace?

Kapitawo ndiye amene ayanganira zinthu za wina. Ife tiri oyanganira ace a Mulungu mcisomo. Zonse zomwe tiri nazo zicokera kwa Mulungu. Buku Lopatulika litiuza kuti Mulungu amationa mmene ticitira zinthu. Mau athu apamtima atiuza bwino bwino zomwe Mulungu ayembekezera kwa ife.

GAWO I:

Kodi cacikhumi ndi ciani comwe Buku Lopatulika lilankhula? Ndi limodzi la magawo

kuti tiyenera kucitila umboni Yesu Kristu.

Coyamba, tiyenera kuonetsa cikondi. Cisanzo ca Yesu Kristu ciyenera kutsatilidwa. "Ndikupatsani inu lamulo latsopano, kuti mukondane wina ndi mnzace; monga ndakonda inu, kuti inunso mukondane wina ndi mnzace." (Yohane 13.34). Kuonetsa cikondi kwa ena cidzaonetsa' ena kuti tiri ophunzira a Yesu. (Yohane 13.35).

Tiyenera kupempherera wina ndi mnzace. Mkristu adzafuna kupempherera anthu ena kwa Mulungu. Citsanzo ticipezanso mwa Paulo. (Werengani Aefeso 1.15-16).

Kusamala kwathu kwa anthu ena kumaphatikizanso mwa thupi ndi za uzimu, Mpingo woyamba unasankha atumiki kuti athandize anthu amene anali kufuna thandizo. Kuthandiza ena sikungatheke ngati tiganiza cabe za thupi. Tiri ndi Yesu amene tiyenera kugawira. **Cikondi** ca Mulungu ciri kwa anthu onse. Tiyenera kutenga Yesu kwa anthu ena.

MTSOGOLERI:

Zinthu zomwe taphunzira lero ziri zoyenera kwa Mkristu aliyense. Moyo wa Mkristu upambana kutsatira cabe malamulo a mkhalidwe wathu. Yesu afuna kukhala wa moyo kupyolera mwa ife. Udindo wathu ndi womwe iye atisankhila kuti ticite masiku onse.

PEMPHERO:



tsa iwo amene akhulupilira mwa Yesu Kristu, mwana wa Mulungu, ndi kukhulupilira mwa iye monga Mpulumutsi.

"Ndipo tidziwa kuti Mwana wa Mulungu wafika, natipatsa ife cidziwitso, kuti tizindikire Woonayo, ndipo tiri mwa Woonayo, mwa Mwana wace Yesu Kristu. Iye ndiye Mulungu woona ndi moyo wosatha." (1 Yohane 5.20) Apa tiri kuona kuti mwana wa Mulungu atipatsa kumvela kapena kudziwa Mulungu. Ndi cikondi cace cimene citidziwitsa ife kuti timdziwe Mulungu. Ndithudi ali Mulungu wabwino.

Kodi tingakhale oona bwanji kuti timdziwa? "Ndipo umo tizindikira kuti tamzindikira Iye, ngati tisunga malamulo ace." (1 Yohane 2.3) Mulungu ali cikondi. Tsono ngati tidziwa Mulungu, tiyenera kukhala ndi cikondi mu mtima mwathu.

Paulo anadziwa Mulungu kuti ali njira yabwino. Iye anati; "Pakuti ndimdziwa Iye amene ndamkhulupilira........." (2 Timoteo 1.12b).

GAWO IV:

Pamene tidziwa kuti Mulungu ndi wabwino conco, tifuna kuti ena amdziwe. Kodi tingacite bwanji ici? Izi ndi zomwe mzimai wina amene ali Mkristu ali kulankhula.

"Mboni yokhulupililika ya Cikristu iri ngati mcere wabwino wa dziko lonse lapansi. Yesu apereka citsanzo ca mcere mu Mateyu 5.13." Anthu onse afuna mcere mndiwo zawo kuti zikhale zokoma pakudya.

Ndiponso anthu afuna mcere monga wa Mkristu kuti ena anthu onse aone Yesu kupyolera mwa iwo. Motero kuti amdziwe monga Mpulumutsi. Aphunzira za Yesu kucokera ku miyoyo yathu. Tikhoza kukhala mboni ya Yesu ngati tidzamtsatira ndi kuphunzira kwa iye."

Onani kuti Mkristu uyu akuti ena akhoza kudziwa Yesu kupyolera mwa ife mmiyoyo yathu.

GAWO V:

Ndi liti pamene munena kuti mudziwa munthu? Tidziwa iye pamene tamuona ndi kukambilana naye. Nanga timudziwa munthuyo bwino ngati tinamuona cabe kamodzi? Iai, tiyenera kukhala ndi iye kwa kanthawi kuti timdizwe bwino.

Cimodzi modzi ndikudziwa Mulungu. Tiyenera kukhala ndi Mulungu kwa nthawi yaitali kuti timudziwe. Tifuna kukhala ndi iwo amene tikonda. Tifuna kukambilana naye. Tifuna kumva zinthu zimene atiuza. Cifukwa cakuti tikonda Mulungu, tifuna kukhala ndi iye kwa kanthawi. "Khalani cete, ndipo dziwani kuti Ine ndine Mulungu, ndidzabuka mwa amitundu, ndidzabuka pa dziko lapansi." (Masalmo 46.10).

Pamene tidziwa Mulungu tifunanso kuti tiwerenge mau ace, ocokera m'Buku Lopatulika, masiku onse. Tifunsa iye kuti akhale ali kulankhula ku mitima yathu pamene tiri kuwerenga. Tifuna kuti tizilankhula kwa iye pa zinthu zimene ziri mmitima yathu. Pamene ticita ici, Mzimu wace udzakhala mwa ife ndi



ali abwino. Ndipo mwamuna ayenera kulamulira ndi cikondi mnyumbamo. Ayenera kuona iye ali mtsogoleri mbanja. Ayenera kukonda mkazi wace monganso Yesu anakonda mpingo.

Ana ayenera kumvelera makolo awo. Koma makolo ayenera kupereka cisanzo cabwino ngati adzafuna kuti ana awapatse ulemu. Kumene kuli cikondi ca ana, kumeneko kudzakhala cimvano ndi ulemu.

GAWO IV:

Mzimai wina analemba izi pa za banja lina lomwe linali loyanganira pa zinthu zomwe linapatsidwa.

"Tidziwa kuti manyumba athu anapatsidwa kwa ife ndi Mulungu. Tiyenera kuyamika Mulungu kamba ka manyumba ndi amuna athu. Mulungu anatipatsanso ana. Izi zonse ndi mphatso zomwe zicokera kwa Mulungu, ndipo tiyenera kumuyamika Mulungu. Kuli anthu ambiri amene nawonso anali kufuna manyumba, koma mwina mwace Mulungu sanawapatse zomwe iwo anali kufuna. Anakalamba opanda nyumba kapena ana. Ife ena amene tiri ndi manyumba kunena kuti tiri ndi mwai. Tsono tiyenera kusunga manyumba athu mosamala monga mzimai amene tiwerenga mu Miyambo 31.10, 11, 28 29. Mzimai uyu ndithudi anasunga nyumba yace bwino, ndipo anali kuzindikila kuti zonsezo zinali mphatso zocokera kwa Mulungu.

GAWO V:

Kodi mkhalidwe wa Akristu uyenera kukhala wotani kwa anthu ena? Mau a Mulungu atiuza

mwini. Ali kutumikila monga mutu kapena mkuru wa chalichi. (Werengani Akolose 1.18-19). Mulungu anasankha Yesu kukhala woyamba kupambana anthu onse.

Ngati Yesu ali kuzindikilitsidwa monga mkuru wa mpingo, tidzafuna kukhala okhulupililirika pano pa dziko lapansi. Mpingo uyenera kutumikila Yesu kuti anthu amene samdziwa amudziwe.

Ciyeneranso kulimbitsa Akristu pamene amakomana ndi kuyanjana mcikondi ca Yesu Kristu. Ife monga oyanganira ace cisomo ca Mulungu, tiyenera kukhala okhulupirika. (Werengani 1 Akorinto 4.2).

Ngati tikhala okhulupirika ku mpingo ici cizatithandiza ife kugwira nchito ya Yesu. (Werengani 2 Timoteo 2.2). Yesu analamulira ophunzira ace kutenga nchito ya mpingo. (Mateyu 28.19-20).

GAWO III:

Kodi mkhalidwe wa Mkristu kubanja uli wotani? Kodi Buku Lopatulika liphunzitsa ciani pa za mabanja aci Kristu? (Werengani Aefeso 5.22-25 ndi Aefeso 6.1).

Muyenera kukhala okomela mtima ena. Ici ciyenera kukhala cinthu cabwino popeza tonse tidziwa Yesu Kristu. Nyumba iri kuchulidwa m'Buku Lopatulika monganso mpingo.

Mnyumba mwamuna ali kulankhulidwa monga mkuru wa nyumba kapena mutu. Ndipo mkazi ayenera kutsatira mwamuna wace mmaganizo omwe



kugwira nchito. Ndipo anthu ena azaona kuti pali kusiyana mmiyoyo yathu. Adzaona Yesu mwa ife.

MTSOGOLERI:

Ciri cabwino kudziwa Mulungu. Buku Lopatulika linenanso kuti Mulungu adziwa amene ali ace. (Werengani Yohane 10.14 ndi 2 Timoteo 2.19).

Tiyeni tithandize ena kudziwa Ambuye wathu Yesu Kristu sabata libwera.

PEMPHERO:

MUTU 2

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: PEMPHERO

MAU APAMTIMA: *"Ndipo Ine ndinena ndi inu, Pemphani, ndipo adzakupatsani; funani, ndipo mudzapeza; gogodani ndipo adzakutsegulirani. Pakuti yense wakupempha alandira; ndi wofunayo apeza; ndi iye amene agogoda adzamtsegulira."*
*Luka 11.9-10*

MTSOGOLERI:

Sabata latha tinaphunzira za kudziwa Ambuye wathu Yesu Kristu. Kodi munali kuganizira za zinthu zoona zomwe tinalankhula Sabata latha? Kodi munalankhula mauwo kwa ana anu ndi banja lonse pa nthawi ya pemphero?

Pamene tilandila Yesu ndi kukhululukilidwa macimo athu, timabwela kudziwa Mulungu. Pamene timdziwa iye, timafuna kulankhula ndi iye. Timafuna kukhala ndi iye kwa kanthawi. (Werenganinso mau apamtima). Yesu atilonjeza kuti ngati tifuna funa tidzapeza Ndipo timadziwa kuti Mulungu amasunga malonjezo ace. Tiyeni tiwerenge Masalmo 63.1. Mlembiyu akuti iye afuna funa Mulungu, nati moyo wace ukumva ludzu la kwa Mulungu. Mu Masalmo 119.10 tiwerenga kuti, "Ndinakufani ndi mtima wanga wonse." (Izi ndi zimene ticita ngati tipemphera. Timafuna funa Mulungu).

GAWO I:

Kodi ndi nthawi iti imene mumakhala ndi



GAWO I:

Pakuganizira za udindo wa kuyanganira moyo wathu wa Cikristu, tiyenera kukhuza Yesu Kristu mu mkhalidwe wathu. Tiyenera kumudziwa iye bwino tsiku ndi tsiku.

Werengani mau amtumwi Paulo mu Afilipi 3.10-11. Paulo ali kulankhula pa za kudziwa Yesu kupyolera mciyanjano. Anafuna kuti amudziwe bwino monga Mpulumutsi wace. Tsono ankaona mphamvu mmoyo wace. Iyi inali mphamvu yomwe inautsa Yesu mmanda.

Ndiponso anafunsanso kuti angakhale ali kuzunzidwa pamodzi ndi Yesu ndi kukhala ngati iye mu imfa yace. Imfa iyi ndi imfa ya cimo. Ngati tifuna kufa ku cimo mu miyoyo yathu, mphamvu ya Mulungu ikhoza kutibweretsela moyo watsopano mwa Yesu Kristu.

Tinaphunzira zambiri za Yesu pamene tiwerenga Buku Lopatulika. Kuphunzira kuyenera kucitika masiku onse. (Werengani 2 Timoteo 2.15).

Pamene tilola Yesu kukhala Ambuye wa miyoyo yathu, timampatsa ulemu ndi kumvelera iye. (Werengani 1 Akorinto 6.19-20). Kumpatsa malo oyamba mmiyoyo yathu kudzatithandiza kuuza ena za iye.

GAWO II:

Mkristu ali nawo udindo wokhuza chalichi. Chalichi ndi guru la okhulupilirika mwa Yesu ndipo ali obatizidwa. Yesu anazipereka yekha ku chalichi. Anagula mpingo ndi mwazi wace

MUTU 10

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESO

COLINGA CA LERO: UDINDO WA MKRISTU MMOYO WACE

MAU APAMTIMA: *"....ndipo udzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ndi mphamvu yako yonse. Laciwiri ndi ili, Udzikonda mnzako monga udzikonda mwini. Palibe lamulo lina lakuposa awa."*
*Marko 12.30-31*

MTSOGOLERI:

Woyanganira ndi munthu amene apatsidwa zina zinthu ndi wina kuti azisunge moyenera. Zinthuzo sizace ai koma kusamala. Ndipo ali nayo mphamvu ya kuona kuti ziri kusungidwa bwino. Mwini zinthuzo adzabwera tsiku lina. Ndipo woyanganirayo azayenera kupereka ripoloti pa zinthuzo.

Mkristu ali woyanganira cisomo ca Mulungu. Alandila cipulumutso ca Mulungu kupyolera mu imfa ya Yesu Kristu pa mtanda.

Pamene tilandila Yesu Kristu mmitima yathu timazipereka ife eni kwa iye. Conco timakhala oyanganira ace a Mulungu. Mulungu anatipatsa moyo kupyolera mmwana wace Yesu Kristu. Tiyenera kulankhula mmene tikhalira mmiyoyo yathu. Tiyenera kuphunzira pa za udindo wa kuyanganira movo wa Mkristu.



pemphero mwa inu nokha? Mlembi wa Masalmo ali kuganizira za nthawi yabwino. (Werengani Masalmo 90.14). Inde tiyenera kuyamba tsiku ndi Mulungu. Pamene tikalibe kulankhula ndi anthu ena, tiyenera kulankhula ndi Mulungu coyamba. Tiyenera kukhala tiri kudzindikila iye pamene tiuka mtulo mmawa mawa.

Pamene sitinayambe nchito ya tsiku, tiyenera coyamba kulankhula kwa Mulungu kuti atitsogolere. Mzimu wace udzatitsogolera m'maganizo athu ndi mmau, ndi mzocita zathu za tsikulo. Ngati sitifunsa iye, sadzatitha-ndiza mnjira iyi. Satikakamiza cifuno comwe anatipatsa. Tiyenera kusankha iye. Ndipo adzatidalitsa mnjira yabwino.

(Werengani Masalmo 9.10) Mlembi wa Masalmo amalankhula za anthu amene adziwa Mulungu, monga mmene tinalankhulira Sabata latha. Amati Mulungu sanakane iwo amene amfunafuna.

GAWO II:

Mwina munazifunsa nokha funso, "Kodi ndingapemphere bwanji?" Kodi kupemphera ndi kufunsa cabe Mulungu zinthu zimene tifuna? Iai, pemphero lipambana apo. Pemphero ndi kulankhulana ndi Mulungu.

Anthu ena anapeza kuti zinthu zinai zotsatirazi ziri zabwino pa za pemphero.

Cinthu coyamba mpemphero ndi kudziwa ici: Yesu ali pano. (Werengani Masalmo 40.16 ndi Masalmo 105.2-5).

Tikhoza kuwelamitsa mitu yathu ndi kuganizira za Yesu. Ndipo timamva kuti ali nafe. Timadziwa kuti ndithudi ali nafe. Pamene tidziwa ndi kuganizira kuti ali nafe, mitima yathu imafuna kuti tipatse moni iye Mulungu. Timapatsa moni munthu aliyense amene tikonda. Ndi cimodzi modzi monga mmene tiganizira za Mulungu ali nafe mcikondi cace.

Kodi Mulungu afuna kuti alankhule ciani kwa ife? Timaganizira pa zinthu zimene Mulungu alankhula kwa ife. Amalankhula kuti: "Mwana wanga, ndi kukonda. Mwana wanga ndi kulandila iwe, monga mmene uliri. Ndi kusunga iwe. Mwana wanga ndikukhululukira cifukwa cakuti ndikukonda."

GAWO III:

Cinthu caciwiri pa za pemphero ndi ici: zikomo Ambuye Mulungu. (Werengani Afilipi 4.4-6).

Yakobo atiuza kuti mphatso iri yonse yabwino icokera kwa Mulungu (Yakobo 1.17). Tidziwa kuti ici ciri coona. Ngakhale mphweya umene tipuma ucokera kwa Mulungu. Mphamvu zomwe tiri nazo zicokera kwa Mulungu.

Kapena cinthu coyamba cimene tidzafuna kulankhula ndi ici: "Zikomo Atate Mulungu pakundikonda." Tsono tikhoza kuchula zinthu zambiri zimene tifuna kuyamika.

Tikhoza kuyamika Mulungu kamba kakuti tiri omasuka kuwerenga Buku Lopatulika, Anthu mu maiko ena (Communist Countries) saloledwa kuwerenga Buku Lopatulika kamba kakuti



Koma kuli malo amene cuma cathu cizasungidwa bwino. (Kambilanani pa za njira imene tingaikilemo cuma cathu kumwamba.)

MTSOGOLERI:

Tiyeni tikumbukilenso mau athu apamtima. (Lankhulani mauwo) Tidziwa kuti zinthu zathu siziri zoyenera m'miyoyo yathu kupambana Mulungu. Mulungu pa kukhala nafe, cikondi, ndi mtendere zinthu izi ziri zoyenera. Tiyenera kuika Mulungu malo oyamba mu umoyo wathu.

Koma Mulungu afuna kuti tikondwere nazo zinthu zomwe atipatsa. "Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu." (Mateyu 6.33).

PEMPHERO:

kupita ku mzimaiyo nthawi zonse, kufunsa iye kuti apange mowa motero kuti agulitse. Tsono mzimai uja amene sanali Mkristu. Anali kupanga mowa ndi kugulitsa. Ndipo ndalama zinali kupatsidwa kwa mzimai amene anali Mkristu.

Tsiku lina azimai ocokera ku mpingo anayendela nyumba ya mzimai amene sanali Mkristu. Ndipo anayamba kukambilana, kuuza mzimai amene ankapulumutsidwila. Anamfunsa kuti abwere ku chalichi, ndi ku msonkhano wa azimai. Mzimai uja anati sindiganizira kuti kuli Cikristu cifukwa cakuti ndi Akristu amene anali kufunsa kuti aphike mowa ndi kugulitsa. Azimai awa anali acisoni ndipo anayamba kupempherera mzimai amene anali wosakhulupirika ndi uja amene anali wotaika."

GAWO V:

Ngati tiri ndi zinthu zambiri, tikhoza kuyesedwa kukhala wodzikonda kamba kazinthuzo. Koma sitiyenera kukhala ndi zinthu zambiri kuti tione kuipa kwace. Tingakhale ndi zinthu zing'ono, koma tiyenera kuziika pamaso pa Mulungu.

(Werengani Mateyu 6.19-21). Tiri kuuzidwa kuika cuma komwe cizakhala kwa nthawi zonse. Mu dziko la palestine, cuma cinali kuikidwa mnsaru za mtengo kwambiri. Ngati njenjetu zinafikako, zinali kusiya zoonongeka. Ifenso tidziwa kuti tikhoza kutaya cuma ngati mbala inadza ndi kutibela.



amati kulibe Mulungu. Ngati anthu ali ndi Buku Lopatulika, ayenera kulibisa. Azimai saloledwa kuphunzitsa ana awo nthano zocokera m'Buku Lopatulika.

GAWO IV:

Cinthu ca citatu ca pa za pemphero ndi ici: Ndithandizeni Mulungu Ambuye. (Werengani 1 Yohane 1.9 ndi Yakobo 5.16). Pamene tibwera pa maso pa Mulungu wathu, timadzindikila za cimo mmoyo wathu. Tidziwa kuti Mulungu amatilandila, ndipo afuna kutikhululukira cinthu ciri conse cimene ciima mnjira yaciyanjano ndi iye. Tsono timafuna kuti Mulungu ationetse cimo mmiyoyo yathu. Ndipo tiyenera kubvomekeza macimowo. Ndipo amatipatsa mtendere mmitima yathu. Sitiyenera kubvomekeza macimo a anthu ena koma aife cabe.

Mzimai wina analemba izi: "Nthawi ya pemphero ndi nthawi imene tilankhula ndi Mulungu. Conco sitiyenera kuleka kupemphera mmanyumba athu. Pemphero liyenera kukhalako masiku onse, monganso nyumba imasesedwa masiku onse. Palibe mzimai amene angakane kusesa nyumba yace masiku onse kuti ikhale yaudongo. Conco timasesa mitima yathu ndi mapemphero, pakubvomekeza macimo athu kwa Mulungu kuti atikhululukile. Tiyeni tikhale ndi nthawi ya pemphero kuti atikhululukile, macimo athu. Tiyeni tipemphere pamene tiri mmabvuto kapena mcikondi."

GAWO V:

Cinthu cacitatu pa za pemphero ndi ici:

Thandizani m'bale wanga. (Werengani Marko 11.22-25).

Pamene tidziwa Mulungu tidzafuna kulankhula kwa iye ndi kukambilana pa za abwenzi athu okondwedwa. Tifuna kupemphelera otaika. Tifuna kuti Mulungu athandize abale athu mmabvuto awo. Cikondi ca Mulungu cimapita kwa ena kupyolera mwa ife pamene tipemphera. (Werengani 1 Timoteo 2.1 ndi Aefeso 6.18).

Iy_ ndi nthano ya mzimai wina watsopano Mcikristu amene anapempherera wina:

Pamene iye anatembenukila kwa Mulungu, amuna ace anamuletsa kupita ku chalichi ndi ku misonkhano ina ya chalichi. Pamene anapita ku msonkhano amuna ace anali kumtsatira mthengo ndi ku mmenya pamaso pa anthu. Koma mzimai anapitilirabe kupita ku misonkhano. Iye anapitilirabe kupempherera amuna ace. Mulungu anayankha mapemphero ace. Lero amuna ace ali Mkristu, ndiponso ena m'banjalo ali Akristu.

MTSOGOLERI:

Tiyeni tikumbukire zinthu zinai izi pamene tipemphera: YESU ALI PANO, ZIKOMO AMBUYE MULUNGU, NDITHANDIZENI AMBUYE MULUNGU, ndi THANDIZANI M'BALE WANGA.

PEMPHERO:



anali wacuma ndikuti anafuna kumanga nkhokwe zazikuru kuti aike zinthu zace. Anaganizira kuti akanakhala kwa zaka zambiri kuti adye zinthuzo. Yesu anati kunali wopusa cifukwa akanafa usikuwo, (Nthanoyi ipezeka mu Luka 12.16-21).

Munthu uyu anacita ngati moyo unali wa thupi lokha. Conco analibe cuma ca uzimu.

Mlaliki anayendela munthu wina. Munthuyo anali ndi nyumba yaikulu imene inali ndi zipinda zambiri. Anali ndi magalimoto atatu. Koma anali wacisoni. Mkazi wace anali mcipatala. Anati nthawi zonse anali kusewenzera ndalama. Tsopano anazindikila kuti munalibe kanthu mu moyo wace. Anati "Ndilibe zinthu zabwino zomwe ndingathe kukumbukila."

GAWO IV:

(Werengani 1 Timoteo 6.7-10. Ndipo kambilanani pa za ndimezo). Ici ndi ciphunzitso cosabvuta, siconco? Timaona coonadi mu anthu masiku ano. Kodi Satana atiyesa ife lero kuika zinthu zathu patsogolo pa Mulungu?

(Werengani Marko 4.19). Ngati mbeu ya mau a Mulungu iri yakufa mmitima yathu, singabale zipatso za iye. Tiri kuuzidwa kuti mau akhoza kuonongedwa ndi zilakolako za dziko lapansi ndi cuma. Kodi tiona coonadici mnthanoyi?

Mzimai wina sanali wokhulupirika Mcikristu cace. Anali kukonda ndalama. Anali ndi bwenzi amene sanali Mkristu. Anali

anakana cifukwa anali wacuma kwambiri. (Mukhoza kuwerenga za izi mu Mateyu 19.16-26). Apa tiona tsoka lalikuru kwa cuma. Cuma cikhoza kuletsa wina kulowa mu ufumu wa kumwamba. Kodi ici citanthauza kuti ife tonse tiyenera kusiya zonse mmalo mwa kuti tipulumutsidwe? Iai, sicitanthauza tero.

Yesu anaona mu mtima mwa munthu uja. Anadziwa kuti munthu uja anakonda cuma kupambana Mulungu. Mmalo mwakuti munthu akhale wophunzira wa Yesu ndi kukhala mwana wa Mulungu, tiyenera kusankha iye Mulungu osati munthu wina kapena cinthu cina. Kulibe njira ina yakuonetsa Mulungu kuti timsankha iye. (Werengani Luka 9.25)

Mulungu atiuza kuti, ".......Cikacuruka cuma musakhazikepo mitima yanu." (Masalmo 62.10b).

GAWO III:

"Kuti, mutadya ndi kukhuta, ndi kumanga nyumba zokoma, ndi kukhalamo; ndipo zidzacuruka ng'ombe zanu, ndi nkhosa zanu, zitacurukanso siliva ndi golidi wanu, zitacurukanso zonse muli nazo; mtima wanu ungatukumuke, nimungaiwale Yehova Mulungu wanu, amene anakuturutsani m'dziko la Aigupto, m'nyumba ya akapolo." (Deutoronomo 8.12-14). Mulungu acenjeza anthu kuti asaiwale iye pamene ali ndi manyumba abwino, zoweta zambiri ndi ndalama zambiri. Pamene anthu akhala ndi zinthu izi lero, amayesedwa kusamila pa ndalama zawo mu banki kuti ziwathandize. Sayamika Mulungu. Koma pamene matenda abwera ndi mabvuto ena mu umoyo wawo, amafunsanso Mulungu.

Yesu anaunzanso za munthu wina amene



MUTU 3

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: KUPEMPHELERA PAMODZI

MAU APAMTIMA: *"Ndiponso ndinena kwa inu kuti ngati awiri a inu abvomerezana pansi pano cinthu ciri conse akacipempha, Atate wanga wa Kumwamba adzawacitira. Pakuti kumene kuli awiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndiri komweko pakati pao."*
*Mateyu 18.19-20*

MTSOGOLERI:

Sabata latha tinalankhula zinthu zitatu zomwe zikhudza pemphero. Kodi mwazigwiritsa nchito Sabata lino pamene munali kupemphera?

Atate wathu Mulungu afuna kulankhula kwa munthu aliyense masiku onse, pamene alibe anthu ena. Ndiponso afunanso ife kusonkhana pamodzi monga ana ace ndi kulankhula kwa iye. Mau apamtima atiuza kuti Yesu Kristu ali ndi mkati mwa pemphero monga anthu amene mungaone.

Pamene tipemphera pamodzi mukhoza kugwiritsa nchito zinthu zinai zimene tinaphunzira Sabata latha. Ndipo, zinthu izi zinalembedwa ndi mzimai amene anazigwilitsira nchito pakati pa anthu amene anali kupemphera pamodzi.

GAWO I:

Zinthuzi zikhoza kugwiritsidwa nchito

nmagulu omwe apempherera pamodzi ochedwa "Pemphero lakulankhula kwa wina ndi mnzace." Ciri ngati guru liri kulankhula ku linzace. Koma pa nthawiyi, aliyense ali kulankhula kwa Yesu, amene ali nawo. Munthu aliyense akhoza kulankhula m'mene afunila.

Mnjirayi munthu amalankhula kwa Ambuye Mulungu pa za nkhani iri yonse imene abweretsa mnthawi ya pemphero. Ngati ndi nthawi ya kuyamika, aliyense akhoza kuima ndi kuyamika Mulungu pa zinthu zosiyana siyana. Ndi nthawi yakugawirana, ndipo anthu ena adzabvomekezana pa za kugawirana pa zimene wina apanga. Izi ndi zomwe mau athu apamtima atiuza kucita.

GAWO II:

Mnjirayi yakupemphererамo, sitiyenera kuopa kukhala cete. Iyi ingakhale nthawi pamene Mzimu Woyera ungakhale uli kulankhula kwa ife. Tsono pamene wina apempherera pa za nkhani ina, timaona kuti cimeneco cinali mmaganizo athu. Uwu ndi Mzimu wa Mulungu umene utitsogolera mpemphero.

Ngati tiri mwa ife tokha, sitidziwa amene tingapempherere. Mulungu mwini atitsogolera. Mulungu anakomana ndi ici pakutumiza Mzimu Woyera ndi kutitsogolera mpemphero. Amatiuza za zimenezi mu Aroma 8.26-27. "Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwini atipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka; 27 ndipo Iye amene asanthula m'mitima adziwa cimene acisamalira Mzimu, cifukwa apempherera oyera mtima monga mwa cifuno ca Mulungu."



bwino? Kodi ciri coipa kukhala ndi nyumba yabwino? Tifuna ana athu kuti akhale ndi zobvala zabwino. Kodi coipa ndi nciani kukhala ndi zinthu zabwino?

Kulibe coipa mwa zinthu izi zokha. Zinthu zoterezi zimapanga moyo kukhala wokondwa. Ndipo Mulungu amatipatsa zinthu zomwe ziri muno mdziko kuti tikondwele nazo. Sanapange cabe cakudya kuti tidye, komanso anacipanga kuti cikhale cotsekemela kuti tikondwere naco pa kudya.

Koma bvuto likhalako pa za zinthu zomwe tiri nazo. Mulungu aticenjeza: "Ndipo munganene m'mtima mwanu, Mphamvu yanga ndi mkono wanga wolimba zinandifunira cuma ici." (Deutoronomo 8.17). Pamene tikalibe kudziwa, timanena mau akuti awa ndi madalitso ocokera mwa ife eni. Tsono kudzikonda kumabwera kwa ife monga mmene tinaphunzilira Sabata latha.

Mulungu aticenjezabe: "Koma mukumbukile Yehova Mulungu wanu, popeza ndi Iyeyu wakupatsani mphamvu yakuonera cuma;....." (Deutoronomo 8.18a). Kodi mungathe kukumbukila ndime yomwe imalankhula cimodzi modzi imene tinaphunzira Sabata latha?

GAWO II:

Munthu wina anabwera kwa Yesu kufunsa mmene ankakhalira ndi moyo wosatha. Yesu anamuuza kuti asunge malamulo. Tsono munthu uja anati anawasunga malamulowo. Tsono Yesu anamuuza kuti agulitse zinthu zace zonse ndi kupatsa ndalama kwa anthu osauka. Munthu uja

MUTU 9

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: CHUMA

MAU APAMTIMA: *"Ndipo Iye anati kwa iwo, Yang'anirani, mudzisungire kupewa msiriro uli wonse; cifukwa moyo wace wa munthu sulingana kucuruka kwa zinthu zace ali nazo."*
*Luka 12.15*

MTSOGOLERI:

(Funsani membala aliyense kuti alankhule ku guru phunziro lomwe lakhala ndi tanthauzo loyenera kwa iye mmiyezi itatuyi).

Mciphunzitso ca Yesu comwe tidzaphunzira lero tidzaona kuti Yesu anali kudziwa mtima wa munthu. Tipeza za ici m'Buku lonse Lopatulika. Mulungu ndithudi amadziwa maganizo a munthu. Anadziwa kuti munthu adzafuna funa cuma.

"Wokhulupirira cuma cace adzagwa; Koma olungama adzaphuka ngati tsamba." (Miyambo 11.28). "Wopindula monyenga abvuta nyumba yace; Koma wakuda mitulo adzakhala ndi moyo." (Miyambo 15.27). Ndime izi zitiuza za zotuluka mkuzinyadila mcuma ndi kukhulupilira mcumaco. Anthu amtundu umenewu adzabweretsa mabvuto ku nyumba zawo.

GAWO I:

Kodi ciri coipa kukhala ndi zinthu za-



Mpemphero tiyenera coyamba kuzipereka mu utsogoleri wa Mzimu Woyera. Kupyolera mu Mzimu Woyera mapemphero akhoza kukhala oyenera kapena a phindu.

Mpemphero liri lonse Mulungu amatengako mbali. Mulungu Atate amamvera. Ndi mdzina la mwana wa Mulungu Yesu Kristu limene tipemphera. Mzimu wa Mulungu umatithandiza pamene tiri kupemphera.

GAWO III:

Ambiri aife tapeza kuti sitipeza comwe tifuna, ngakhale pamene tifunsa cinthu cina kupatsidwa kwa wina. Ndi cifukwa ninji ici cirimotere? Kupeza vankho tiyenera kudziwa kuti tiri ana a Mulungu wa mmwamba.

Tiyeni tiganizire za ana athu okha. Kodi tiwapatsa zinthu zomwe iwo afuna nthawi zonse? Kodi tiwalola kucita zinthu zomwe iwo afuna kucita? Tidziwa kuti ngati iwo adzadya maswiti ambiri otsekemela pa nthawi imodzi akhoza kudwala. Conco timawaletsa kuti asadye kwambiri. Tidziwa kuti izi siziri bwino. Ndipo timawaletsa kuwapatsa maswiti ambiri pa nthawi imodzi. Timacita ici kamba kakuti tiwakonda.

Ciri cimodzi modzi ndi Atate wathu wakumwamba. Sitingaone za mtsogolo monga iye adziwira. Amadziwa zinthu zambiri zomwe ife sitidziwa. Conco amayankha mapemphero mnjira yomwe adziwa kuti idzakhala bwino kwa ife.

GAWO IV:

Ngati pemphero lathu likhuza munthu wina, tiyeni tikumbukira kuti Mulungu sakakamiza kuti anthu amtsatire. Adzamvera mapemphero athu ndipo Mzimu Woyera udzafuna funa munthuyo amene ali wotaika ndi kubwera mu mtima mwace.

Ngati tidzapitilirabe, adzapitilira kucita tero. Mwina munthu uja wotaika adzabwera kulandila cikondi ca Mulungu. Tiyenera kupempherera mabanja athu ndi abwenzi. Tiyenera kupemphera kuti Mulungu adzawathandiza mbvuto lawo ndi kupanga zolinga zawo.

Sitiyenera kukaikila Mulungu pamene tiri kupemphera. (Werengani Ahebri 11.6) Apa tiwerenga kuti Mulungu amapatsa iwo amene akhulupilira ndi kufuna funa iye. Tiyenera kukhulupilira ndi mitima yathu yonse. Mpemphero timafunadi Mulungu. Mphatso zomwe atipatsa sizingakhale zomwe ife tinali kufuna, koma timadziwa kuti adzatipatsa zabwino.

GAWO V:

Mzimai wina anapereka umboni uwu pa za kupemphera pa banja. "Ici cakhala cinthu cabwino pa banja pathu kukhala pamodzi mu mzimu. Uli mpata wabwino m'banja. Kuimba nyimbo kwakhala kotikondweletsa mnthawi ya mapemphero mbanja lathu. Tipeza uthenga kucokera mnyimbo ndi pa kuwerenga Buku Lopatulika. Kupemphera pa banja kutithandiza kukambilana pa za mabvuto omwe ana amakhala nawo muno mdziko.

Pemphero lapa banja likhoza kuyanjanitsa



kupatsidwa kwa anthu a Mulungu. Tiyeni tione zofunikila ku madalitso a Mulungu. Coyamba tiyenera kudzicepetsa. Tiyenera kukumbukira kuti mwa ife tokha palibe comwe cilimo.

Cinanso ndi cakuti tiyenera kupemphera. Tiyenera kufuna funa mphamvu ya Mulungu ndi nzeru osati za ife eni. Tiyenera kufuna funa nkhope yace. Mulungu sadzatikakamiza kupita kwa iye. Tiyenera ife eni kufuna ndi kumvera iye. Koma amalankhula kuti ngati tifuna, tidzapeza.

Ndipo tiyenera kucoka ku njira zathu zoipa. Ucimo m'moyo wa Mkristu umalanda madalitso a Mulungu. Angakhale Mkristu sangathe kudziteteza ku cimo mu umoyo wace mphamvu za iye yekha. Mulungu atipatsa kale kupambana cilango ca macimo athu. Tsopano adzatipatsa mphamvu kupambana macimo ngati tidzazicepetsa, kupemphera, kufuna funa nkhope yace, ndi kucoka ku njira zathu zoipa. (Werengani Aroma 6.6).

MTSOGOLERI:

Satana amatiyesa kwambiri pa za kudzikonda. Mwina tingadzikonde ife eni kamba ka manyumba athu kapena ndalama zomwe timakhala nazo. Kapena zobvala zimene timabvala, kapena ana. Kapena nchito imene tigwira. Kapena nchito imene tigwilira Mulungu. Ngati Satana tigwira mzonsezo za kudzikonda, iye amatinyenga kuti tisalandile madalitso a Mulungu.

PEMPHERO:

Makolo pamodzi ndi mpingo unapempherera ana aja. Mulungu analankhula kwa mtsikana, ndipo anapereka moyo wace kwa Mulungu. Mtsikanayo anaimilira kutsogolo kwa chalichi ndi kubvomekeza macimo ace nalila kwambiri. Mtsikano winanso anabvomekeza macimo ace. Analankhula pa za mmene anali kumwelela mowa, cigololo ndi kusamvelera makolo ace, Mulungu anampulumutsa. "Nsembe za Mulungu ndizo mzimu wosweka; Inu, Mulungu, simudzaupeputsa mtima wosweka ndi wolapa." (Masalmo 51.17)

GAWO VI:

Yesu analankhula pa za kudzicepetsa. Iyenso anali wodzicepetsa. "Ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzicepetsa vekha. nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda." (Afilipi 2.8). Anali kumvelera Atate wace wakumwamba. Tinaphunzira Sabata latha kuti kumvera kubweletsa mtendere.

Tiyenera kutsatira cisanzo ca Yesu. "musacite kanthu monga mwa cotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pace, komatu ndi kudzicepetsa mtima, yense ayese anzace omposa iye mwini." (Afilipi 2.3). Sitiyenera kucita zinthu kamba kodzikonda kapena kuganizira kuti tiri akuru kupambana ena. Sitiyenera kuziganizira kuti tiri abwino kupambana ena.

"Ndipo anthu anga ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapempnera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhululukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao." (2 Mbiri 7.14). Uthengawu uli



kamba kakuti ngati onse abwera pamodzi ndiye kuyamba kwace kwaciyanjano. Mumalola Mulungu kuti alankhule kwa iwo. Ndithudi mukhoza kukambilana zinthu momasuka pa banja. Mkhoza kuwazindikilitsa kuti afuna kupulumutsidwa kucokera kumacimo awo.

Ndi nthawi ya pemphero yomwe mungathe kuphunzitsa ana anu kupemphera maka maka ngati sanapempherepo kale. Mulungu amalankhula kwa anthu osiyana siyana ndi kudalitsa iwo mosiyananso. Pempheronso limatipatsa mpata wa kugawirana. Yesani ici ndipo mudzadabwitsidwa. Patsani aliyense m'banja lanu cocita nthawi ya kupemphera. Ana ayenera kuthandiza kuyimba. Kapena ayenera kuwerenga Buku Lopatulika. Aliyense ayenera kupemphera pa yekha. Izi zinthu zikhoza kupanga mapemphero anu bwino."

MTSOGOLERI:

Tiyeni tiwerengenso ndi kuphunzira zinthu pa za mapemphero pomwe tiri pa nyumba. Tiyeni tigawireko mabanja athu.

PEMPHERO:

MUTU 4

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: UFUMU WA MULUNGU

MAU APAMTIMA: *"Odala ali osauka mumzimu; cifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba."*
*Mateyu 5.3*

MTSOGOLERI:

Mmasabata apitawo takhala tiri kuona kuti ndi cinthu cabwino kotani, kudziwa Mulungu. Pamene timdziwa iye, tifuna kutenga kanthawi kukhala ndi iye. Tifuna kupemphera mwa ife eni masiku onse. Tifunanso kupemphera pamodzi ndi banja lathu. Tifuna kupemphera ndi Akristu anzathu.

Lero tidzaphunzira za ciphunzitso cina ca Yesu. Pamene tiwerenga Buku Lopatulika tiona kuti Yesu analankhula za ufumu wa Mulungu. Mwina munadabwa cimene ici citanthauza. Yohane m'batizi analalikila kwa anthu kuti atembenuke mitima popeza ufumu wakumwamba wayandikila. Kodi anatanthauza ciani apa?

GAWO I:

Pamene tiganizira za ufumu, tidziwa kuti kuyenera kukhala Mfumu. Mfumuyo imalamulila onse amene akhala mu ufumuwo. Conco citanthauza kuti Mulungu ali mfumu kwa onse amene ali ace.

Kunali anthu ambiri mnthawi ya Yesu amene anaganiza kuti Yesu anabwera kuika ufumu wa muno mdziko lapansi. Anafuna kuti amenyane



Nthanoyi itiphunzitsa kuti palibe munthu amene ali wodzikonda amene iye angathe kupemphera mcoonadi. Munthu wina anati khomo la kumwamba liri laling'ono motero kuti palibe munthu amene angalowe pokhapo ngati iye adzagwada.

Palibe munthu angapemphere ngati iye ali kunena anthu ena. Pemphero loona ndi lakuonetsa miyoyo yathu kwa Mulungu, koma osati kufanizila ndi anthu anzathu.

GAWO V:

Mmalo mwakudziwa Mulungu ndi kupulumutsidwa, munthu aliyense ayenera kudzicepetsa ndi kubvomekeza macimo ace. Pamene adziwa kuti alibe mphamvu ya kuzipulumutsa, Mulungu tsono akhoza kugwira nchito.

Nthano pansipa ionetsa ici:

"Pali mtsogoleri wa azimai amene anathandiza atsikana kukula bwino. Koma atsikanawo sanali omvera. Anawo sanali kumvera mai wawo motero kuti ngati amai awo asonkha moto mmawa mawa ana aja amakhalabe ali kugona. Sanali kupatsa ulemu ngakhale bambo wawo.

Pamene mtsikana wamng'ono anauzidwa kupita kuchalichi, iye ankanalankhula moipa mwina kutaya Buku Lopatulika. Mtsikanayo anathawa ndi mnyamata wina motero kuti akwatilane ici cinali cinthu ca manyazi mmudzi muja. Ndipo linalinso bvuto ku mpingo.

ukuru? Yesu anaphunzitsa kuti wodzicepetsa uja adzakhala wamkuru. Anati tiyenera kukhala ngati ana.

GAWO III:

Yesu analankhula pa za atsogoleri acipembezo mu nthawi yace mu Mateyu 28.1-12. "Muyenera kucita zinthu zimene anena," anawauza, "ngakhale kuti iwo sakucita zimenezo. Osatsatira njira zawo." Yesu anati anacita zinthu zawo zabwino kuti anthu awaone, koma anaika mabvuto ambiri pa anthu ena. Zinthu zosungilamo ndime zocokera m'Buku Lopatulika zinali zazikuru kuti ena azione. Anakonda malo abwino okhalamo ndipo anakonda kuitanidwa ndi maina abwino oyenera. Kodi nafenso tipeza macimowo m'miyoyo yathu?

GAWO IV:

Yesu analankhulanso nthano ina mu Luka 18.9-14 pa za anthu awiri amene anali kupemphera. Mfarisi amene anapita kukapemphera anali wozikonda ndipo ananena ena. Koma sanapite kukapemphera moona. Anapita kukauza Mulungu ubwino umene iye anali nawo. Ndi cifukwa cace analankhula zinthu zimene anafuna kulankhula. Koma funso silakuti "Kodi sindili wabwino monga anthu ena?" Koma kuti "Kodi ndili wabwino monga Mulungu?" Pamene tiziyangana mwa ife tokha pa maso pa Mulungu, kulibe malo akudzikonda.

Wamsonkho uja anadziwa kuti anali wocimwa. Anafunsa Mulungu kuti amumvera cifundo.



ndi asilikali aci Roma amene anatenga dziko lawo. Koma Yesu anati "Ufumu wanga suli wa dziko lino lapansi........." (Yohane 18.36).

Kodi munthu akhala bwanji mu ufumu wa Mulungu? Yesu Kristu anati, "....Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona "Ufumu wa Mulungu." (Yohane 3.3b) Kodi mukumbukila zomwe tinaphunzira musabata latha kuti munthu ali wakufa mu mzimu cifukwa ca macimo ace? "Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zocimwa zanu, zimene munayendamo kale........" (Aefeso 2.1, 2a) Pamene munthu alandila Yesu Kristu, mtengo wa macimo ace,tsono amatsukidwa, Mzimu wa Mulungu ukhoza kubwera ndi kukhala mwa iye mu mtima. Mnjirayi ali wobadwa wace wa Mulungu ndipo amakhala mu ufumu wa Mulungu.

GAWO II:

Ciphunzitso coyenera ca Yesu cipezeka mu mau apamtima. Kodi atanthauza ciani? Yesu anali kulankhula kuti tiyenera coyamba kudziwa kuti tiri osauka mu mzimu pamene sitinakhale ku mbali ya ufumu wakumwamba.

Tiyenera kudziwa kuti palibe cinthu ciri conse comwe tingacite kuti tizipulumutse. Tiribe cuma ca uzimu. Sitingagwiritse nchito ndalama kapena mphamvu, kapena kucita nchito zabwino kuti tilowe mu ufumu wa Mulungu. Pamene tidziwa ici coonadi mumtima wathu, tsono tikhoza kulola kuti mphamvu ya Mulungu ilamulile miyoyo yathu. Ndi Mulungu yekha amene angatipulumutse kucokera ku cilango ca macimo athu ndi kukhala obadwanso mu ufumu wa Mulungu.

Kumene kuli ufumu tidziwa kuti mfumu iri ndi mphamvu. Imalamulila anthu. Conco ngati tikhala mu ufumu wa Mulungu, Mulungu ayenera kutilamulila.

GAWO III:

Kodi Akristu amalola kuti mfumu yawo iwalamulile? Kodi mumalola Mulungu kuti alamulile moyo wanu masiku onse?

Mau athu apamtima ali kulankhulanso kwa Akristu. Tiyenera kudziwa kuti tilibe cuma ca uzimu comwe tingakhale naco masiku onse. Tiyenera kufunsa Mzimu wa Mulungu kuti utsogolere miyoyo yathu. Tifuna kuti Mulungu akhale mfumu yathu kulamulira mitima yathu. Akhoza kutipulumutsa kucokera ku mphamvu ya ucimo tsiku, lililonse. (Werengani Aroma 6.6-7). Kambilanani pa za zimenezi).

Koma nthawi zambiri Akristu amakhala tsiku ndi tsiku wopanda mphamvu ya Mulungu. Tiyenera kuzindikira mphamvu za satana kuti akhoza kutipereka mziyeso. Satana ali wa mphamvu kupambana ife. Conco sitingathe kukhala ndi moyo wopambana kopanda mphamvu yocokera kwa Mulungu.

Tiyenera kuphunzira phunziro lomwe Paulo anaphunzira. "Pakuti cabwino cimene ndicifuna, sindicicita; koma coipa cimene sindicifuna, cimeneco ndicicita." (Aroma 7.19). Anaphunzira kuti munalibe cabwino mwa iye, ngakhale pamene anakhala mwana wa Mulungu. Cabwino mwa ife ndi Mzimu wa Mulungu umene ukhala mwa ana ace.



Maganizo awa amatiika pamwamba. Sapatsa ulemu Mulungu ndi kuzindikila kuti zonse zomwe tiri nazo zinapatsidwa kwa ife ndi Mulungu. (Werengani buku la Yakobo 1.17 kudzikuza kuti panga ife kukhala opambana Mulungu. Tidziika ife eni pa mpando wacifumu wa Mulungu. Timaswa lamulo loyamba (Eksodo 20.3). Sitiyenera kuika cinthu ciri conse patsogolo pa Mulungu. (Werengani Luka 14.26).

Mulungu adzalanga anthu odzikhuza. "Maso a munthu akuyang'anira kumwamba adzatsitsidwa, ndi kudzikweza kwa anthu kudzaweramitsidwa pansi; ndipo Yehova yekha adzakwezedwa tsiku limenelo." (Yesaya 2.11)

Mulungu adzadalitsa anthu amene adzicepetsa (Werengani Yesaya 4.10). Ciri cinthu cabwino kwa Mulungu kukhala ndi anthu.

GAWO II:

Kodi kudzikuza kumeneku kuonetsedwa bwanji mmitima yathu? Yesu analankhula za nthano ya madyelero ya ukwati mu Luka 14.7-11. Unali mwambo wa anthu oitanidwa kukhala pafupi ndi iwo amene anali kukwatilana. Yesu anaphunzitsa kuti cinali cinthu cabwino kukhala pansi ndi kufunsidwa kupita kukakhala pa mpando wabwino kupambana munthu mwini kuzisankhila malo okhala popeza ciri cinthu comvetsa manyazi kucoka pa mpando ndi kukhala pansi.

Ophunzira a Yesu anali kutsutsana ndani amene adzakhala mkuru mu ufumu wa Mulungu. (Werengani Luka 9.46-48). Kodi anthu masiku ano afuna kukhala "oyamba mciwerengelo?" Kodi ciphunzitso ca Yesu cinali cotani pa za

MUTU 8

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: KUDZICEPETSA

MAU APAMTIMA: *"Cifukwa munthu aliyense wakudzikuza adzacepetsedwa; ndipo wakudzicepetsa adzakulitsidwa."*
*Luka 14.11*

MTSOGOLERI:

Sabata latha tinaphunzira njira ya ku cikondwelero ndiyo yakumvera Mulungu. Kodi takhala tiri kugawira mabanja athu za zoonadi zimenezi?

Lero tidzaphunzira za cinthu cina cimene Yesu anaphunzitsa kwambiri. Timawerenga za cimeneci m'Buku Lopatulika. (Werengani Miyambo 16.19 ndi Miyambo 29.23) Kodi mukhoza kukamba kucokera mndimezi cinthuco? Inde tirikulankhula za kudzicepetsa.

Kodi ndi cifukwa ninji kudzicepetsa kuli koyenera. Miyambo 15.33b tiuzidwa kuti "Ndipo cipatso citsogolera ulemu."

GAWO I:

Munthu wokudzikuza amacimwila Mulungu. Kodi ici ciri bwanji tere? Kodi ndi cifukwa ninji kudzikonda kumagawanitsa munthu kucoka kwa Mulungu? Ine ife tonse ciri coyenera kuti tiziyang'ana mwa ife tokha ndi kudalila nyumba yathu ndi zinthu zomwe tiri nazo. Pakuti tinadzigulira tokha ndi kuzisewenzera.



GAWO IV:

Kodi muganizira kuti Kristu amadziwa kuti ali osauka mu mzimu? Kodi amafunsa mphamvu ya Mulungu kuti idzale mwa iwo tsiku ndi tsiku? Kodi inu mumacita ici?

Mzimai wina analemba izi:

"Mzimai wina amene anali membala wa chalichi anali munthu wakumwa mowa ndipo moyo wace unali wobvuta ku chalichi. Analeka kupita ku chalichi ndipo sanapite ku misonkhano ya azimai. Anali kukhala ku nyumba ya mowa nthawi zambiri. Koma pamene Mulungu analankhula kwa iye anabvomekeza macimo ace. Lero ali okondwa ndi amuna ace ngakhale kuti iwo amuna sali Mkristu. Ali wokondwa kamba kakuona mphamvu ya Mulungu. Tsopano ali kucitira umboni Yesu Kristu kwa amuna ace."

Pamene mzimai uyu anamvelera Mulungu. Mphamvu ya Mulungu inapambana mayeso a Satana.

GAWO V:

(Werengani Mateyu 13.44). Mnthawi ya Yesu kunalibe nyumba zosungilamo ndalama (banks). Anthu anaika ndalama zawo pansi. Pamene munthu anapeza ndalama pansi, anagulitsa zonse zomwe anali nazo zinthu kuti agule munda ndi ndalamazo. Yesu anati ufumu wa Mulungu uli ngati mmenemo. Pamene tiona kuti ciri cokondweletsa kuti Mulungu alamulile miyoyo yathu, tidzakhoza kusiya njira zathu zozikonda.

Mzimai wina analemba izi pa za banja lomwe linalola Mulungu kuti akhale ali kulamulila miyoyo yawo.

"Kunali nyumba kumene anthu anasiya kutsatira Mulungu. Ana sanafune zinthu zokhuza Mulungu. Sanamvere munthu aliyense. Tsiku lina makolo anapemphera usiku wonse. Mmawa mwace anthu a m'banja muja anamvera mphamvu ya Mulungu iri kugwiritsidwa nchito. Ana anabvomekeza macimo awo ndi ucimo wa kusamvera. Ndipo mzimu wa Mulungu unadzadza mwa iwo. Lero kuli cikondwerelo pa nyumba ndi ku chalichi."

MTSOGOLERI:

Tiyeni titenge zinthu zoonadi zomwe taphunzira kumanyumba athu. Tiyeni tiganizire pa zonsezo. Tiyeni tifunse Mulungu kuti azigwiritse nchito mmiyoyo yathu.

PEMPHERO:



MTSOGOLERI:

Kuli lamulo lomwe Yesu anapereka posiliza ulaliki wace. Lamuloli liri kupezeka mu Yohane 15.17,"Zinthu izi ndilamulira inu, kuti mukondane wina ndi mnzace." Kodi tikonda Akristu anzathu? Ciri cobvuta kukonda anthu. Kuli anthu ena amene sakondedwa. Kuli anthu amene acita zinthu zakutiwawa, Koma Mulungu satiuza kuti ndi anthu oti. Koma afuna ife kuti tiwakonde. Kodi tingacite bwanji ici pakuti ciri cinthu cobvuta?

Tikhoza kufunsa Mulungu kuti atipatse cikondi mmitima yathu kuti tikonde anthu ena. Pamene tifunsa Mulungu kuti atipatse mphamvu yakukonda ena, tsono Mulungu adzagwira nchito. Adzaika cikondi cace ife kuti tikonde anzathu. Tsono cikondici cidzapita ku mitima ina. Yesani cimeneci ndipo mudzapeza mtendere.

PEMPHERO:

GAWO V:

"Odala ali akuzunzidwa cifukwa ca cilungamo: cifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba." (Mateyu 5.10). Cioneka ngati ciri cinthu cacilendo kuti ngati munthu azunzidwa adzakhala wokondwa, sitero? Koma ici ndi comwe Yesu ananena. Timaona za coonadi cimeneci mmalo ena. (Werengani Yakobo 1.2,3 ndi Aroma 5.3,4). Tiri kuuzidwa kuti mayeso amabweletsa kupilira ndipo miyoyo yathu imakhala yoyenera.

"M'menemo mukondwera, kungakhale tsopano kanthawi, ngati kuyenera, mukacitidwe cisoni ndi mayesero a mitundu mitundu, kuti mayesedwe a cikhulupiriro canu, ndiwo a mtengo wace woposa wa golidi amene angotayika, ngakhale ayesedwa ndi moto, akapezedwe ocitira ciyamiko ndi ulemerero ndi ulemu pa bvumbulutso la Yesu Kristu;" (1 Petro 1.6-8)

Tiri kuuzidwa kuti miyeso itionetsa ife ngati tiri ndi cikhulupiriro coona kapena co-nama. Kodi mudziwa munthu wina amene analeka kupita ku chalichi kamba ka milandu yomwe inamgwera? Ngati tikhulupilira mwa Mulungu, adzaona kuti tipambana muyeso uli wonse mu umoyo wathu. Adzapanga cikhulupiliro cathu kukhala colimba.

Kuli milandu yambiri kapena miyeso. Muyeso wina ndi matenda. Wina ndi kulankhulana ndi munthu wobvuta. Mukhoza kuchula miyeso ina. Ngati zinthu izi zibwera mmoyo wathu tiyenera kufunsa Mulungu kuti "Kodi mundiphunzitsa ciani mzonsozi."



MUTU 5

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: KUUNIKA

MAU APAMTIMA: *"Pamenepo Yesu analankhulanso nao, nenena, Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi; iye wonditsata Ine sadzayenda mumdima, koma adzakhala nako kuunika kwa moyo."*

*Yohane 8.12*

MTSOGOLERI:

Monga mmene taphunzilira ziphunzitso za Yesu, taphunziranso kuti ciri cabwino kudziwa Mulungu. Ciri cabwino kukhala ndi nthawi ya kulankhula naye kupyolera mpemphero ndi kulamulila mitima yathu. Lero tidzaphunzira za kuunika. Yesu analankhula za kuunika. Tionanso kuti kuunika ku kumapezeka m'Buku Lopatulika lonse.

Coyamba ndi cakuti, tiyenera kudziwa kuti mdima ndi pomwe sitinaone kuunika. Panali mdima pano pa dziko lonse lapansi (Genesis 1.2). Tsono Mulungu anati, "Kuyere ndipo kunayera." Kuunika kuli kwabwino. Tidziwa kuti zomela sizingathe kumela ngati kulibe kuunika. Kuunika kumatithandiza ife kuona ndi kuti ticite nchito yathu.

GAWO I:

Nthawi zina ana amakhala ndi mantha ndi mdima. Sadziwa kuti ciri pafupi ndi citi mumdima. Ngakhale akuru amaopa mdima nthawi

zina. Amadziwa kuti anthu ena amabisala mu mdima kuti abele ena zinthu kapena kucita zinthu zina zoipa.

Cimo lomwe liri mumtima mwa munthu limapanga iye kuti ali mumdima. (Werengani Miyambo 4.19). Tonsefe tidziwa kuti mdima wa cimo uli cimodzi modzi.

Kodi ndi cifukwa ninji anthu amakhala mu mdima wa macimo? Buku la 2 Akorinto 4.4 litipatsa yankho. (Werengani ndimeyi) Kodi Mulungu ndani pano pa dziko lapansi nthawi ino? Ndi Satana. Iye aphimba maso a okhulupirika maganizo awo kuti akhalebe mumdima. Iyeyo Satana ndiye mulungu wa dziko lino lapansi amene achulidwa mu ndimeyi.

Kodi tiona tsopano mphamvu yomwe Mulungu wa dziko lapansi ali nayo? Akhoza kulankhula ku maganizo athu. Ici ndi cifukwa cace tiyenera kufunsa Mulungu kuti atsogolere maganizo athu. Ndi Mulungu yekha amene angacotse maganizo oipa a Satana mwa ife. Nthawi zina tiganizira za kuganiza maganizo oipa amene aikidwa ndi Satana mwa ife. Tifuna kukhala wodzikonda. Tifuna kukhala tiri kucitira nsanje munthu wina. Tsono maganizo awa oipa amakhala malankhulidwe oipa. Ndipo kulankhulako kumaipa. Kodi muona mmene Satana akuyeselani? Njira yokha yakupambanilamo Satana ndi kufunsa Mulungu kuti atsogolere miyoyo yanu monga tinalankhulira kaya kuphunzira Sabata latha.

GAWO II:

Mulungu ali nalo yankho ku ucimo wa



Tsopano mwamunayu ali kubwera ku chalichi kamba kathandizo lomwe linaperekedwa kwa iye ndi ife azimai. Akhala ali kulimbitsidwa kwambiri pakubwera ku chalichi. Tikhulupilira kuti Mulungu amathandiza ngati tidzafunsa iye kuti atithandize."

GAWO IV:

(Werengani Aefeso 4.32). Kodi muganizira mzimai uyu analikumvela zimene Mulungu ananena m'ndimeyi?

"Mzimai wina anali kukalipa msanga msanga. Ngati apita kunyumba ana anali kukhala cete ndipo iye anali kukhala wosakondwa. Pomwe mwamuna wace anali kufunsa, anali kucita ngati adzampanda cabe. Mulungu analankhula kwa iye. Lero muli cikondwelero mnyumba yawo."

Njira yapafupi imene ticimwilamo ndi mmene tikambila zinthu. "Kotero lilimenso liri ciwalo cacing'ono, ndipo lidzikuzira zazikuru. Taonani kamoto kakang'ono kayatsa nkhuni zambiri! Koma lilime palibe munthu akhoza kulizoloweretsa; liri coipa cotakataka, lodzala ndi ululu wakupha." (Yakobo 3.5,8). Mundime ya 8 tiwerenga kuti palibe munthu amene angathe kuzoloweretsa lilime. Ndi Mulungu yekha amene angathe. Adzalamulira lilime lathu ngati tamfunsa iye kuti atero.

Onani mnthanoyi kuti Mulungu anaonetsa mzimaiyu cimo lace. (Werengani Yakobo 5.17) pamene anamvelera Mulungu, mtendere unabwera mnyumba.

ndipo ali kumvelera. Werengani Masalmo 119.10).

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse." (1 Yohane 1.9).

"Munthu m'modzi wa iwo amene analandila Yesu mumzinda mwathu pa nthawi ya citsitsimutso ndi mtsikana. Iye sanamve zimene anthu anali kulankhula pa za Yesu Kristu. Iye anatsatira bwenzi lace la mwamuna kuli konse komwe mwamunayo anapita cifukwa anali woliza gatala. Pamene Ambuye analankhula ku mtima wace, anabvomekeza macimo ace. Tsopano ali mtsikana wokondwa kwambiri mwa Ambuye Yesu Kristu, izi ndi zomwe ali kulankhula."

GAWO III:

Kodi mukumbukila mau amene apezeka mu Mateyu mutu 25 pa za kucita zabwino kwa Yesu pamene ticitaizi kwa anthu ena? Kodi muganizira kuti mzimai uyu anamvelera ziphunzitso za Yesu m'mauwo?

"Mzimai wina anali wokhulupirika amene anabatizidwa mchalichi yathu, koma amuna ace sanali wokhulupirika. Amuna ace sanagwire nchito kokwanila miyezi isanu ndi umodzi. Tsono ife azimai tinamva cisoni kwa mnzathu kuti anali mmabvuto. Tinasonkna ufa ndipo tinasonkhanso ndalama kuti tithandize iye kwa miyeziyo yomwe mwamuna sanali kugwira nchito. Mulungu anayankha pemphero lathu ndipo mwamunayo anapeza nchito.



mumdima. "Anthu amene ayenda mumdima, aona kuwala kwakukuru; iwo amene anakhala m'dziko la mthunzi wa imfa, kuwala kwaturukira kwa iwo." (Yesaya 9.2) Aneneri anadziwa pa zakubwera kwa kuunika. Yohane atiuza mu Yohane 1.4,5 "Mwa Iye munali moyo; ndi moyowu unali kuunika kwa anthu. Ndipo kuunikaku kunawala mumdima; ndi mdimawu sunakuzindikira." Onani mundimezi kuti mdima siunapambane kuunika. Mdima citanthauza cimo ndi ulamulilo wa Satana. Satana sangapambane Yesu, yemwe ali kuunika, ngati ife tizapereka ulamulilo wa ife eni kwa Mfumu yathu.

"Ndadza Ine kuunika ku dziko lapansi, kuti yense wokhulupirira Ine asakhale mumdima." (Yohane 12.46). (Werenganinso mau apamtima alero). Awa ndi malonjezo abwino.

Tsiku lina mlembi wa bukuli anakomana ndi mwamuna wa mnzace. Nkhope yace inaoneka ngati inali yophimbidwa ndi mitambo. Ndipo sanaoneke ngati anali wokondwa. Patapita miyezi, ndinaonanso munthuyu. Pa nthawiyi anaoneka mosiyana ndi kale lija. Nkhope yace inali yowala ndipo wokondwa. Anali kumwemweta mwemweta. Anali kukonda anthu ena.

Kodi ndi ciani comwe cinacitika kwa iye? Pamene ndinafunsa mkazi wace, iye anati, "Tinali ndi msonkhano wa citsitsimutso mchalichi yathu. Iye anatembenuka ndipo anakhala Mkristu. Moyo wace unasintha kucokera pa nthawiyo."

GAWO III:

Timadziwa kuti Yesu ali kuunika kwa muno mdizko lapansi. Komanso anati, "Muli kuunika kwa dziko lapansi." (Mateyu 5.14a) (Werenganinso 1 Atesalonika 5.5). Ngati tiri ana akuunika, tiyenera kukhala motani muno mdziko? Yesu atiuza, (Werengani Luka 11.35) "Potero yang'anira kuunika kuli mwa iwe kungakhale mdima." (Werengani Aefeso 5.8,9).

Kodi ana a Mulungu amakhala monga ana akuunika? Kodi mitima yathu iri yoyera ndi kuti tiri okondwa kuona anthu anzathu? Kapena tiri ndi mbali zina m'moyo wathu zimene tifuna kuti zikhale zobisika?

Kodi ndi cifukwa ninji tifuna kuti zinthu zina zomwe tinakamba zikhale zobisika kapena zina zomwe ticita? (Werengani Yohane 3.20,21) "Pakuti yense wakucita zoipa adana nako kuunika, ndipo sakudza kwa kuunika, kuti zingatsutsidwe nchito zace. Koma wocita coonadi adza kukuunika, kuti nchito zace zionekere kuti zinacitidwa mwa Mulungu."

GAWO IV:

Ciri cinthu cacisoni kuti zocita za Mkristu zimakhala za mumdima kupambana kukhala kukuunika.

Mzimai wina ali kulankhula nthanoyi:

"Sindidzaiwala nkhope ya mwamuna wa mzimai amene tiphunzira naye, nkhopeyo iri yosakondwa." Mwamunayo anati, "Mkazi wanga anathawa!" Ndinakumbukila mkazi wace bwino bwino. Anali wacangu ndiponso wa nchito yabwino, ndipo wokhulupirika mwa Yesu Kristu.



iye kumene tiyenera kuyangana monga pa za thandizo. (Werengani Masalmo 146.5).

"Pakuti ufumu wa Mulungu sukhala cakudya ndi cakumwa,koma cilungamo, ndi mtendere, ndi cimwemwe mwa Mzimu Woyera." (Aroma 14.17). Ndimeyi itiuza kuti ufumu wa Mulungu umabweletsa cikondi ndi mtendere. Pamene tiri mu ufumu wa Mulungu ndi kulola iye kuti alamulile miyoyo yathu, timadziwa cikondwelero coona. Kodi munaciona ici? "Izi ndalankhula ndi inu, kuti cimwemwe canga cikhale mwa inu, ndi kuti cimwemwe canu cidzale." (Yohane 15.11).

GAWO II:

Tiyeni tione zimene Yesu atiphunzitsa mu mau apamtima. Amatiuza kuti tidzakhala okondwa ngati tidzamva mau a Mulungu ndi kuwasunga. Pamene tikonda munthu wina, timalankhula kwa iye ndiponso munthuyo amalankhulanso kwa ife. Timamvera ku zomwe amalankhula.

, Ici ciri cimodzi modzi ndi mkhalidwe wathu ndi Mulungu. Timamvetsera ku zomwe amalankhula kwa ife kupyolera mmau ace, Buku Lopatulika. Timamvera iye pamene timalankhula ndi iye kupyolera mpemphero tsiku ndi tsiku. Pamene tipemphera sitilankhula mau onse mwa ife tokha. Kodi mukumbukila kuti pamene tipemphera sitiyenera kuopa kukhala cete? Tiyenera kuima ndi kukhala cete mwapang'ono kuti Mulungu alankhule kwa ife.

Yesu Kristu atiuza kuti anthu okondwa ndi iwo amene amamva zimene iye ali kulankhula,

MUTU 7

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: CIKONDWELERO

MAU APAMTIMA: *"Koma Iye anati, Inde, koma odala iwo akumva mau a Mulungu, nawasunga."*
*Luka 11.28*

MTSOGOLERI:

(Chulani ziphunzitso za Yesu zomwe taphunzira kale.) Sitiyenera kukhala wopanda Mzimu wa Mulungu monga munthu uja amene tinaphunzira Sabata latha. Mmalo mwace tiyenera kudzadzidwa ndi cikondi kapena Mzimu wa Mulungu.

Lero tidzaganizira za cikondwelero. Tonsefe tifuna kukhala okondwa. Kodi ndi ciani comwe citipanga kukhala okondwa? Ngati tiri ndi ndalama zambiri zakugulira zinthu, kodi ici cidzatikondweletsa? Anthu ambiri amaganiza tero. Koma anthu ambiri amene ali olemela amakhala wosakondwa m'mitima yawo.

Tidzaona mmene mau a Mulungu alankhulila pa za cikondwelero.

GAWO I:

M'buku la Masalmo 144.15b tiwerenga kuti "....Odala anthu amene Mulungu wao ndi Yehova!" Ndimeyi itiuza zomwe tinaphunzira poyamba: kuti kudziwa Mulungu ciri cinthu cabwino comwe cingacitike kwa ife. Cimabweretsa cikondwelero coyenera mmitima yathu. Ndi kwa



Ndidziwa kuti anapatsidwa masiku kukalila malilo a wina wacibale amene anamwalira kumudzi kwa miyezi itatu.

Anabwerera pa Sabata. Sabata lotsatira sanabwere ku chalichi. Kodi ndi ciani comwe cinacitika? Abale a mwamuna anamuuza kuti mkazi wace anakhala masiku ang'ono. Pamene anali pa chuti anali kubwela kukumana ndi mwamuna amene anasiyana naye kale ndipo anasiila mwamunayo ana awiri. Iye anasiya banja la ana asanu ndi kupita kukatenga ana awiri.

(Werengani Afilipi 2.14,15) "Citani zonse kopanda madandaulo ndi makani, kuti mukakhale osalakwa ndi oona, ana a Mulungu opanda cirema pakati pa mbadwo wokhotakhota ndi wopotoka, mwa iwo amene muonekera monga mauniko m'dziko lapansi." Apa tiri kuuzidwa kuti tiyenera kuunika monga nyali mdziko lapansi lino la ucimo. Anthu otaika ayenera kuona Yesu mwa ife pamene asanabwere kwa Yesu.

GAWO V:

"Ndipo uwu ndi uthenga tidaumva kwa Iye, ndipo tiulalikira kwa inu, kuti Mulungu ndiye kuunika, ndipo mwa Iye monse mulibe mdima. Tikati kuti tiyanjana ndi Iye, ndipo tiyenda mumdima, tinama, ndipo siticita coonadi. Koma ngati tiyenda m'kuunika, monga Iye ali m'kuunika, tiyanjana wina ndi mnzace, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wace utisambitsa kuticotsera ucimo wonse." (1 Yohane 1.5-7) Sitinganene kuti tiri mciyanjano ndi ca Mulungu ngati tiyenda mumdima.

"Iye amene anena kuti ali m'kuunika, namuda mbale wace, ali mumdima kufikira tsopano lino. Iye amene akonda mbale wace akhala m'kuunika, ndipo mwa iye mulibe cokhumudwitsa. Koma iye wakumuda mbale wace ali mumdima, nayenda mumdima ndipo sadziwa kumene amukako, pakuti mdima wamdetsa maso ace." (1 Yohane 2.9-11. Kambilanani pa za ndimezi).

Nthano pansipa ionetsa azimai kuti ali kuyenda mkuunika pakusamalira odwala:

"Nchito imodzi ya azimai ndi kupempherera odwala mcipatala. Ife azimai timakomana ndi kukambilana kuti ndi tsiku liti lomwe tingapite kukacezera anthu odwala. Timaganizira kuti ndani amene adzapemphera ndi kuwerenga Buku Lopatulika. Ngati tonse takomana ndi kubvomekezana pa zomwe tizacita, timapita ku cipatala kukapempherera pamodzi ndikuwerenga Buku Lopatulika."

MTSOGOLERI:

Tiyenera kuziona mwa ife tokha ndi kudziwa kapena tiyenda mumdima kapena mkuunika. Tiyenera kuzindikila kuti sitingayende mkuunika mphamvu ya ife eni, tiyenera kutembenukira mitima yathu kwa Yesu Kristu. (Werengani Masalmo 27.1).

PEMPHERO:



kusoka zobvala tsikulo la Sabata lonse. Mwamsanga anayamba kumwa mowa. Ndipo anayamba kuona azimai ena mmalo mwa mkazi wace.

Tsono timaona mmene zinthu zoipa zimapambanila pamene sitili wodzadzidwa ndi Mzimu wa Mulungu.

(Werenganinso mau apamtima ndipo lankhulani pa za tanthauzo la mauwo).

(Werengani Mateyu 25.31-40 kunyumba, Fotokozani kwa mamembala mmene muganizira zomwe zalankhulidwa mndimezi mmene mizimu yoipa ingacokele, kudzikonda, ndi kusilila zinthu za eni ndi zina zace). (Werengani 1 Akorinto 15.58).

MTSOGOLERI:

Tiri azimai acikristu. Tiyeni tiwerenge za mzimai wa Mulungu mu Miyambo 31.27.

Tidziwa kuti kuli njira imodzi yakukhalilamo wokondwa mu umoyo. Iyi ndi njira yakutenga nthawi ndi kulankhula ndi Mulungu kupyolera mpemphero. Tiyenera kufunsa Mulungu kuti alamulile maganizo athu tsiku liri lonse. Tiyeneradi kufunsa Mulungu kuti atitsogolere mmau abwino ndi mzinchito zathu. Tsono tidzadzadzidwa ndi cikondi. Tidzadzadzidwa ndi zinthu zabwino za Mulungu. Ngati tizafunsa Mulungu kuticitira cabwino, Mulungu adzatero.

PEMPHERO:

GAWO IV:

Mzimai wina ali kulankhula nthanoyi ya wina mzimai amene analeka kupemphera:

"Tsiku lina azimai anayendela mzimai wina amene analeka kusonkhana ndi azimai ena pa tsiku lacinai. Anafunsa mzimaiyo ndi cifukwa ninji sanali kubwela ku msonkhano wa azimai kapena ku chalichi pa tsiku la Sabata. Mzimai uja anayamba kupereka mayankho kuti iye anali kudwala kwa masiku ambiri. Azimai awiri anayesa kuthandiza mzimai uja namuwerengela mau a Mulungu kucokela m'buku la Yeremiya 3.19.

Koma mzimai uja anali kuphika mowa ndi kugulitsa. Pamene anagulitsa mowa wace anatenga ndalama ndi kuika mnkhokwe ya cimanga. Pamene anatero, akhoswe anabwera nadya ndalama za mapepala zokwanila K26.00. Mzimai uja sanadziwe cimene akanacita. Anatenga ndalama za mapepala zodyewa dyewa ndi akhoswe napita kusitolo ali kuthamanga. Koma mwini sitolo sanalole kuti asinthanitse ndalamazo kamba kakuti manambara kunalibe pakuti akhoswe anadya. Mzimaiyu anabwera kuchalichi ndi kubvomekeza cimo lace," (Werengani Miyambo 22.8)

GAWO V:

Kwa zaka zambiri mbiri munthu wina anali kubwera ku chalichi nthawi zonse. Koma moyo wace siunali wodzadzidwa ndi zinthu za Mulungu. Anayamba kusoka zobvala pa tsiku la Sabata mmadzulo kuti apeze ndalama zapadela. Anasiya tsopano kupita kuchalichi ndi kuyamba



MUTU 6

COLINGA CA MIYEZI ITATU: ZIPHUNZITSO ZA YESU

COLINGA CA LERO: NGOZI MMOYO WOPANDA MZIMU

MAU APAMTIMA: *".....Ndi kuzama nciani; ndi kuzindira cikondi ca Kristu, cakuposa mazindikiridwe, kuti mukadzazidwe kufikira cidzalo conse ca Mulungu."*
*Aefeso 3.19*

MTSOGOLERI:

Takhala tiri kuphunzira ziphunzitso za Yesu. Atiphunzitsa kuti ciri cinthu cabwino kudziwa Mulungu. Ciri cinthu cabwino kutenga nthawi kukhala ndi iye kupyolera mpemphero ndi kulola iye kulamulira miyoyo yathu. Tauzidwa kuti tiyenera kuyenda mkuunika monga iye ali kuunika.

Lero tidzaphunzira zinthu zomwe zipezeka mnthano yomwe Yesu Kristu analankhula mu Luka 11.24-26.

Iyi ndi nthano ya cisoni. Mzimu woipa unacotsedwa mwa munthu wina. Pomwe mzimu woipawo unabwelera kwa munthu uja, unapeza kuti mmoyo wa munthu uja unatsukidwa wonse, koma siunazalidwe ndi kanthu kali konse ai. Conco mzimuwo unapita ndi kutenganso mizimu yoipa isani ndi iwiri. Conco inadza ndipo inalowa mwa munthu uja. Tiyeni tsono tiganizire za tanthauzo la nthanoyi.

GAWO I:

Tiphunzira kucokera ku nthanoyi kuti moyo wa munthu siungakhale wopanda kanthu kali konse. Pamene munthu akhala Mkristu, adzafuna kusiya maganizo ace oipa ndi zocita zina. Adzafuna kusiya njira zakale. Tsono moyo wace ukhala woyera. Koma siuyenera kukhala wopanda kudzadziwa ndi Mzimu Woyera.

Moyo wopanda mzimu ndi moyo wotaika. Sicili cokwanila kunena kuti sitizacita ici, ndipo sitiyenera kucita cija cinthu. Tiyenera kuganiza maganizo abwino. Tiyenera kupanga zocita zabwino. Tiyenera kucita zinchito zabwino. Tsono zinthuzi zikhoza kutenga malo a zija zakale. Kulibe malo azinthu zoipa, mizimu yoipa, kudzikonda konse, kubweleranso ku moyo.

Munthu wina anati pamene mucotsa namsongole, anamsongole awiri adzamela pa malopo. Tiyenera kufesa maluwa kaya mbeu zina mmalo mwace. Tsono mbeu izi zabwino zimamela mmalo a mbeu zoipa namsongole.

GAWO II:

Mzimai wina analemba izi mu msonkhano wa azimai:

"Azimai ambiri ali kuyenda mnjira ziwiri. Iwo sanazipereke okha kwa Mulungu ndi mitima yawo yonse. Pamene iwo amadwala kwa nthawi yaitali, amaganiza kubwerera ku njira za dziko. Posilizira pace amati Mulungu alibe mphamvu ya mizimu yoipa.

Ena, pamene atembenuka, amafoketsedwa



pakumwa mowa ndi kukoka fodya kapena kupembeza mizimu. Ena amaganiza kuti sangakhale ndi nchito yabwino kapena kupita ku msonkhano wa azimai. Sadziwa kuti mizimu yawo ifuna cakudya, monganso thupi lifuna nyama ndi kukula. Ngati sitipembeza Mulungu mmisonkhano ya chalichi, mizimu yathu siingakule. Idzakhala yofoka kamba kakuti siitenga cakudya ca moyo."

Mzimai uyu ali woona. Tiyenera kutenga nthawi yakuwerenga Buku Lopatulika, kupemphera ndi kupembeza ndi Akristu ena. Conco miyoyo yathu siizakhala yopanda mzimu. Izadzalidwa ndi maganizo abwino. Izi zidzakula mmaganizo abwino. Zoipa zizacotsedwa.

GAWO III:

Sicili cokwanila kucotsa zoipa cabe. Cabwino ciyenera kulowa. (Werengani Aefeso 5.18) Munthu adzadzadzidwa ndi mzimu. Ngati ali wodzadzidwa ndi maganizo abwino, ndiye kuti maganizo oipa amacotsedwa.

Ngati coipa cacotsedwa ndipo munthu safuna kuika zinthu zabwino, tsono alibe nchito. Kuli mwambi wakuti, "Maganizo opanda nchito ndi momwe Satana agwirira nchito." Ici ciri coona.

Nthawi zambiri timabvutika ndi maganizo oipa. Ngati tidzabwezanso mwa ife tokha, "Sindiyenera kuganiza za cija," timaika maganizo athu pa cimeneco nthawi ndi nthawi. Coipa cikhoza kucotsedwa pakuganizira cabwino. Sitikhala cabe anthu abwino ngati tikana cabe kucita zinthu zoipa. Tikhala anthu abwino pakuika zinthu zabwino mmoyo wathu.